Chidziwitso: Alimi Ayenera Kudziwa za Matenda a Chitopa ndi Katemera wa I-2



Chitopa ndi matenda oopysa zedi, amene akhoza kupewedwa pogwiritsa ntchito katemera wa I-2. Katemerayu amapezeka ku Central Veterinary Laboratory ku Lilongwe, ku ma veterinary shops, kapena kwa alangizi a boma. Katemerayu aperekedwe pakatha miyezi inayi iliyonse.

Palibe mankhwala ochiza chitopa. Chikafika chitopa pa mudzi, nkhuku zambiri zimafa, pokhapokha ngati zinalandirapo katemera kale.

Katemera sachiza chitopa, koma amatchinjiriza chitopa ku nkhuku zathu ndi kuzipatsa chitetezo asanabwere matendawa kwathu.

Katemera sagwira ntchito nthawi yomweyo. Chitetezo chimabwera pang'onopang'ono kufikira sabata, ndipo chimapitirira kuteteza nkhuku kwa miyezi inayi.

Alimi asamadikire chitopa chifike. Chifukwa akatero nkhuku zawo zidzafabe zambiri pokhapokha ngati zinalandirapo kale katemera.

Alangizi a ku midzi asapereke katemera ku nkhuku zodwala. Ngati nkhuku zikudwala, thupi lake limakhala lofooka, ndiye katemera sangathe kugwira ntchito bwino m'thupi lofooka. Ndiye nkhuku zimafabe. Ngati atemera nkhuku zodwala ndi kufa mlimi adzataya chikhulupiliro kwa alangizi. Pazifukwa izi alangizi aja asapereke katemera ku nkhuku zodwala.

Alimi adziwe kuti katemera wa chitopa ndi wa nkhuku iliyonse yaing'ono kapena yaikulu. Ngati katemera angaperekedwe kwa nkhuku zochepa, zotsalazo zifabe.

Chizindikiro cha botolo la katemera chimaoneka chonchi:

Central Veterinary Laboratory Mw
I-2 Newcastle Disease Live Vaccine
300 doses Store at 4-8°C
Administer by eye drop
Batch No. 000 Exp Date: 00/0000
For animal use only

Onetsetsani kuti botolo silinatsegulidwe kale. Komanso werengeni bwino tsiku lotha ntchito la katemerayu.

Copyright © 2013-2020 Rural Poultry Centre - All rights reserved
Copyright and linking policy «» Privacy policy «» Terms and conditions «» FAQ
Site last reviewed 30 December 2021